Global Storybooks


globalstorybooks.net

## Nkhuku ndi Bongololo

Winny Asara
Magriet Brink
Sitwe Benson Mkandawire, David Mwanza

This work is licensed under a Creative Commons Attribution 3.0 International License.
https://creativecommons.org/licenses/by/3.0


# Nkhuku ndi Bongololo



Winny Asara
Magriet Brink
Sitwe Benson Mkandawire, David Mwanza

3

Chichewa ny



Nkhuku ndi Bongololo anali abwenzi. Koma anali kukonda kupikisana. Tsiku lina, anaganiza kuchaya m’pila wa myendo kuti aone ngati katswili ndi ndani.



Anayenda kubwalo la m'pila ndipo anayamba masewera awo. Nkhuku inafulumira, koma Bongololo anafulumira kopambana. Nkhuku inachaila kutali koma bongololo anachaila kutali mopambana. Nkhuku inayamba kukalipa.



Anagaza kuti achaye mapenoti. Bongololo anayabila kukhala wogwila m’pila. Nkhuku inamwesa cigoli cimodzi. Tsopano inali nthawi yankhuku kuti igwile m’pila.





Kucokela apo, Bongololo ndi Nkhuku anakhala adani.



Nkhuku inakhosomola kufikira itakhosomolela panja Bongololo amene anali mumimba mwake. Bongololo ndi amai ake anakalawa ndi kukwela m’tengo kubisala.





Bongololo anachaya ndipo anamwetsa. Bongololo ananyunya ndi kumwetsa. Bongololo anamwesanso ndi mutu. Bongololo anamwetsa zigoli zisanu.



Nkhuka inakalipa kuti inagonja. Inagonja kothelathu. Bongololo anayamba kuseka cifukwa ca madandaulo amuzake pambuyo pakugonja.






Nkhuku inageya. Ndipo inamela ndi kutaya mata. Ndipo inakhosomola. Bongololo anali kunyansisa.



Amake Bongololo anakuwa nati, “Sewenzesa mphamvu zako zapadela mwana wanga!” Bongololo atha kununkha ndi kusamveka bwino. Nkhuku inayamba kumvela kudwala.






Nkhuku inakalipa kwambiri ndikusengula kamwa namela bongololo.



Pamene nkhuku inali kuyenda kunyumba, inakumana ndi amake abongololo. Amake Bongololo anafunsa nati, “Kodi wamuonako mwana wanga?” Nkhuku siyinalankhule ciliconse. Amake Bongololo anada nkhawa.





Amake Bongololo anamva kaliu kakang’ono. “Ndithandizeni amai!”, liu linalila. Amake Bongololo anayangana uku ndi uku, ndi kumvetsetsa ndi cidwi. Mau anacokera mumimba mwa nkhuku.